

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

MUYENERA KUBADWANSO

Mkati mwa usiku wina, munthu wina dzina lake Nikodemo anatuluka kukafunafuna Yesu. Nikodemo anali wa mgulu la akulu olamulira achiyuda lotchedwa Sanhedrini. Pokhala Mfarisi, iye ankakhulupirira zomatsatira Chilamulo cha Mose kwathunthu. Ulendo wake kupita kwa Yesu unali wachinsinsi, popeza Iye anali munthu waudindo komanso anali wolamulira wachiyuda.

Nikodemo anamutchula Yesu kuti “Rabi,” dzina laulemu kwa aphunzitsi achiyuda. Iye anavomereza kuti Yesu anatumidwa ndi Mulungu chifukwa cha zozizwitsa zimene anachita. Yesu anayankha Nikodemo ndi mau amene akhala akumveka kwa zaka mazana ambiri. Mau amenewo amatsutsa mitima ndi maganizo kuti afunefune china choposa chimene dzikoli lingapereke. “Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu.”

Chilungamo chenicheni, mtendere, ndi chisangalalo m'dziko lino lapansi ndi moyo wamuyaya m'moyo ukubwerawo zimene zili mphatso za ufumu wa Mulungu sizingapezeke popanda kubadwanso kwauzimu. “Kubadwanso mwatsopano” kumatanthauza kusintha kwauzimu. Sikusinthika kwa thupi koma ntchito ya umulungu ya Mulungu yomwe amatsitsimutsa moyo.

Kubadwa kumatanthauza chiyambi. Monga kubadwa kwathupi kumationetsera ife moyo wapadziko lapansi, kubadwa kwauzimu ndi chizindikiro cha chiyambi cha kuyenda mwauzimu ndi Ambuye. Kubadwa kwauzimu kumeneku sikubwera chifukwa chakuti talowa m'gulu lachipembedzo, kusinthika kwa makhalidwe, kapena kutengera kakhaliidwe kabwino, kapenanso kukhazikika pa miyambo ina ya zipembedzo. Kubadwa mwatsopano ndi ntchito ya Yesu Khristu.

Anthu akaika chikhulupiriro chawo mu imfa yodzikhuthula ndi kuuka kwa Yesu Khristu, amene ali Mwana wa Mulungu, Iyeyo amawakhululukira machimo ndi kuwayanjanitsa ndi Mulungu. Kubadwanso, kapena kubadwa mwatsopano, kumatheka ndi mphamvu yaumulungu ya Mulungu. Iye amakonzanso mitima yathu ndi kutipanga tikhala zolengedwa zatsopano. Mphamvu ya uchimo imasweka, ndipo anthu obadwanso mwatsopano atha kukhala mu ufulu ndi chiyero cha Yesu Khristu, osati chifukwa cha mphamvu zao, koma chifukwa cha kusinthika kwa umulungu mwa mphamvu ya Mulungu.

Chipulumutso chimatsamira pa kubadwanso kwauzimu, ndipo popanda kutero anthu amakhalabe akufa mwauzimu ndi otalikana ndi Mulungu. Kupembedza pakokha m'mzikiti, m'kachisi, m'chihema, kapena m'nyumba yopemphereramo sikuchititsa kuti munthu abadwe mwatsopano. Otsatira achipembedzo ambiri sanakhalepo ndi kubadwa kwauzimu kumene Yesu anakunena. Anauza Nikodemo kuti, “Ngati munthu sabadwa mwatsopano...” Posatengera za kuchuluka kwachuma, uzimu, dziko, zaka, kuti ndi mwamuna kapena mkazi, kapena chipembedzo chake, ONSE akuyenera kubadwa mu uzimu kuti alandire moyo wosatha. Kungodziwa kuti Khristu ndi Mesiya sikukwanira. Kusintha kwakukulu kwa kubadwa mwatsopano ndikofunikira. Kubadwanso kumatanthauza “kubadwanso kachiwiri,” komanso “kubadwa kuchokera kumwamba.” Chifukwa chake, kubadwa kwauzimu sikungovomereza Khristu kapena kunena kuti uli wochimwa, koma ndi pamene moyo umasinthidwa kuchoka ku uchimo ndi chidetso kupita ku chilungamo ndi chiyero. Kubadwa kwauzimu kumeneku si kochitika chifukwa cha khama la munthu. Ndi kubadwa kwaumulungu,

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Chipulumutso chimatsamira pa kubadwanso kwauzimu, ndipo popanda kutero anthu amakhalabe akufa mwauzimu ndi otalikana ndi Mulungu.”

Mau a Mkonzi

Kalozera pophunzira
Baibulo: Kubadwa
Mwauzimu

Kuchokera ku imfa
kupita ku moyo

Funso Yanko

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

kwa nthawi yomweyo mwamzimu kumene kumachitika kudzera m'ntchito yaumulungu ya Mulungu.

Ana akabadwa, amatengera makhalidwe a makolo awo. Chimodzimodzinso, anthu akabadwa mwatsopano, umunthu wao umasantha, ndipo amakhala ana a Mulungu. Salinso omangidwa ndi chikhalidwe chachibadwa cha uchimo koma ali ogawana nawo chikhalidwe cha umulungu, ndipo ali ndi mphamvu limodzi ndi Mulungu yakugonjetsa uchimo.

Yesu anauza Nikodemo mu Yohane 3:6, “Chobadwa m’thupi chikhala thupi, ndipo chobadwa mwa Mzimu, chikhala mzimu.” Kubadwa mwathupi kuli monga mwa thupi ndipo ntchito zathu ndi zochita zathu zimakhala zathupi, komabe pali kubadwa kwina. Icho chimene chili chobadwa mwa Mzimu wa Mulungu chili chazimu.

“Kubadwa mwatsopano...
ndiko kutsitsimuka
kwauzimu, mwai
wachiwiri, ndi lonjezo
la chiyembekezo
chamuyaya.”

Zili zomvetisa chisoni kuti anthu ambiri amafuna kukwaniritsa zofuna za moyo kudzera mu zokhumba zathupi lauchimo, mabungwe a anthu, zipembedzo, ndi nzeru za anthu. Monga tinabadwa m’thupi, TIYENERA kukhala ndi kubadwa kwauzimu.

Kubadwa mwatsopano kuli koposa chiphunzitso chaumulungu. Kuli kuitanidwa ndi kuukhala moyo

wosinthika kwambiri zomwe zimaposa kwambiri chimene uchimo ndi chipembedzo zingapereke. Ndiko kutsitsimuka kwauzimu, mwai wachiwiri, ndi lonjezo la chiyembekezo chamuyaya.

Kodi munabadwa kwatsopano? Njira YOKHAYO yolandirira moyo wosatha ndiyo kudzera mu kubadwa kwauzimu. Tsegulani mtima wanu ndi kuika chikhulupiriro chanu mwa Ambuye Yesu monga Mwana wa Mulungu. Khulupirirani ntchito ya kuombola ya Yesu amene anafera pa mtanda chifukwa cha machimo anu. Vomerezani kuti uzimu wanu uli wopanda kanthu, lapani ndi kusiya machimo anu, ndi kupereka moyo wanu kwa Mulungu. Itanani Yesu kuti akhale Mbuye ndi Mpulumutsi wa moyo wanu. Pamene muchita zimenezo, Iye adzachita chozizwitsa cha kubadwa kwauzimu, ndipo moyo wanu udzasandulika kuchoka ku imfa kupita ku moyo. ■



Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m’dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Zosati zochokera m'ntchito za m'chilungamo, zimene tidazichita ife, komatu monga mwa chifundo chake anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonedwe a Mzimu. — Tito 3:5

Ifeyo tingathe kupulumutsidwa chifukwa cha chifundo ndi chikondi cha Mulungu. Palibe wina aliyense mwa ife amene ayenera kupulumutsidwa, koma chili mphatso yochokera kwa Mulungu. Sitiyenera kuchita nkondo kuti tilandire mphatso, chifukwa monga mwa dzina lake, mphatso imaperekedwa kwaulere. Yesu anabwera padziko lapansi ndi kudzipereka yekha monga nsembe kuti tiyeretse dwe ku uchimo ndi kulandira moyo wosatha. Mphatso ya chipulumutso imeneyi ndi yamtengo wapatali kwambiri kuposa zosangalatsa ndi chuma cha m'dzikoli.

Mutu wathu ulendo uno ndi wa, “Kubadwa Mwauzimu,” ndipo ukuulula choonadi chakuya chaumulungu ndi kuchitapo kanthu mwa kubadwanso mwatsopano. Pamene ndimaunguza Malemba, ndinachitanso mantha ndi kuoneka mophweka komanso mphamvu ya uthenga wabwino.

Kubadwa mwatsopano ndi lingaliro losamvetsetseka kwa zikhulupiro ndi zipembedzo zambiri. Zipembedzo zambiri zimaphunzitsa kuti kupeza kuwala kapena kuvomerezedwa ndi Mulungu zimachitika chifukwa munthu wagwira ntchito ndipo wamamatira ku malamulo. Anthu amayesetsa kupeza chimwemwe ndi chitetezo cha moyo wosatha. Kuti munthu amasuke ku ukapolo wa uchimo ndi kulowa mu ufumu wodabwitsa wa Mulungu, pakuyenera kukhala kusinthika kwa moyo. Chodabwitsa cha chipulumutso sichimatheka kudzera mu chilungamo chathu koma kudzera mu kubadwanso kwauzimu. Ngakhale pali mfundo zofunika za m'Malemba zakuti tizitsatire, ntchito zathupi zachilungamo sizitipulumutsa.

Kuchita nawo ntchito za mpingo, kukhala membala wa mpingo, kukhala ndi moyo wa makhalidwe abwino, kupemphera, kuphunzira malemba, kupereka, ndi kutumikira ena izi sizibweretsa chipulumutso. Chipulumutso chimafuna ntchito yaumulungu ya Mulungu. Kubadwa mwatsopano kutanthauza kuti Mulungu akuchita m'miyoyo yathu zomwe ifeyo sitingathe kudzichitira tokha. Kubadwa kwauzimu ndikofunikira kwa onse. Ana amene anakulira m'banja lachikhristu amafunikanso kubadwa mwatsopano monga mmene amachitira ana akunjia.

Kubadwa kwauzimu kumabweretsa kusinthika. Chinachake chimachitika chomwe nthawi zambiri sitingathe kuchifotokoza. Mwa mphamvu ya Mulungu machimo athu amakhululukidwa, mitima yathu imayeretsedwa, ndipo miyoyo yathu imamasulidwa ku temberero la imfa. Mulungu alemekezeke chifukwa cha kubadwa mwatsopano!

Pali chitonthozo chachikulu pakukhala wobadwa mwatsopano. Pamene tikupitiriza kugonjera ku chifuniro cha Mulungu ndi kupereka miyoyo yathu kwa Iye, pali mtendere podziwa kuti ndife ana a Mulungu. Tidzalkwitsabe pamene tikukula, koma tidzakhala omasuka ku uchimo. Tikhoza kupumula mu chisomo chopulumutsa cha Khristu ndi mu chidziwitso chakuti tinabadwa—ndife amoyo, osinthika, ndi okhululukidwa.

Ngakhale kuti ndimasangalala kudziwa tanthauzo la kubadwa kwauzimu, mtima wanga ulirira anthu amene akuyesetsa kuti ayanjane ndi Mulungu chifukwa cha khama lawo. Kulimbikira kumeneku ndi kuyesetsa kopanda pake komwe kumalephera kufika pa chiyero chenicheni. Chilichonse kupatula kubadwa mwatsopano ndi chokumana nacho chomvetsa chisoni. Chilungamo chenicheni, mtendere, ndi chisangalalo zimabwera chifukwa cholowa mu ufumu wa Mulungu kudzera mu kubadwanso kwauzimu.

Pemphero langa ndi lakuti uthenga wakubadwa kwatsopano ufike kwa otayika ndikupitiriza kusintha miyoyo.

Michael W. Smith

July 2024



Mukafuna kutipeza


pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.





Kalozera pophonzira Baibulo

Mutu: Kubadwa Mwauzimu

Kuwerenga Malemba:

Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sangathe kuona Ufumu wa Mulungu. — Yohane 3:3

Mwachidule:

Anthu onse ali pansu pa chilango cha imfa chifukwa cha uchimo. Kuti munthu alowe mu ufumu wa Mulungu kumafunika kuti moyo wake udzutsidwe kuuzimu, kusinthika kumeneku kumachitika ndi mphamvu ya Mulungu. Kubadwa kwa uzimu kumeneku kumayeretsa moyo ku uchimo ndi kutipatsa mphamvu yakuti tikhale otenga nawo gawo mu chikhalidwe cha umulungu.

I. Imfa Yauzimu

- A. Aroma 5:12 Imfa inafikira pa anthu onse.
- B. Aroma 3:23-24 Onse anachimwa.
- C. Aroma 6:23 Mphoto yake ya uchimo ndi imfa.

II. Kutembenuka

- A. Machitidwe 3:19 Lapani ndipo tembenukani.
- B. Mateyu 18:3 Mukapanda kutembenuka.

III. Kubadwa mwatsopano

- A. Yohane 3:1-8 Pokhapokha ngati munthu abadwa mwatsopano.
- B. 1 Petro 1:23 Mubadwense ndi mbewu yosavunda.

IV. Cholengedwa chatsopano

- A. 2 Akorinto 5:17 Wolengedwa watsopano mwa Khristu.
- B. Yesaya 1:18 Kuyeretsedwa ku uchimo.

V. Kubadwanso kwatsopano

- A. Tito 3:5 Kusambitsidwa kuti tibadwense kwatsopano.
- B. Ezekiele 36:24-27 Mtima watsopano ndi mzimu watsopano.

VI. Kubadwa mwauzimu ndi chifuniro cha Mulungu

- A. Yohane 1:12-13 Obadwa osati ndi chifuniro cha munthu.

- B. Aefeso 2:8-10 Chipulumutso ndi mphatso ya Mulungu.

VII. Chiwombolo

- A. 1 Petro 1:18-19 Osaomboledwa ndi zinthu.
- B. Agalatiya 6:15 Si mdulidwe kapena kusadulidwa.

VIII. Munthu Wauzimu

- A. 2 Akorinto 4:16 Munthu wamkati akonzedwa kwatsopano.
- B. Akolose 3:9-11 Valani munthu watsopano.

IX. Chikhalidwe chaumulungu

- A. 2 Petro 1:3-4 Ogawana nawo chikhalidwe chaumulungu.
- B. Aefeso 4:24 Munthu watsopano wolengedwa m'chiyero.
- C. Agalatiya 5:19-24 Ntchito za thupi zisiyana ndi ntchito za Mzimu.

X. Umboni wa kubadwa mwatsopano

- A. 1 Yohane 3:9 Sachita tchimo.
- B. 1 Yohane 5:4 Agonjetsa dziko lapansi.
- C. 1 Yoh. 2:29 Amachita chilungamo.

XI. Kudziwika ndi kukula mwa Khristu

- A. Aefeso 3:14-17 Banja limatchedwa ndi dzina la Atate.
- B. Aefeso 4:15 Kukula mwa Khristu.

Kumaliza

*Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa
ndi zolakwa, ndi zochimwa zanu. — Aefeso 2:1*



Kuchokera ku imfa kupita ku moyo

Pachiyambi cha chilengedwe, Mulungu anaumba anthu, nawapatsa osati thupi lanyama ndi mwazi lokha komanso mzimu wosafa. Komabe, anthu anaudetsa mzimuwo ndi uchimo, nadzibweretsera temberero lonse la imfa yakuthupi ndi yauzimu. Komabe, Mulungu anaika kubadwa kwauzimu ngati njira yowaombolera ndi kuti apulumuke ku mphamvu ya uchimo ndi lamulo la imfa.

“Kupitirira pa kubadwa kwachilengedwe, pali kubadwa kwauzimu komwe kumasintha ndi kusanduliza mzimu wa munthu.... Mulungu amasintha zinthu zonyansa, zosalungama, ndi zoipitsidwa ndi uchimo kuti zikhale zoyera, zaukhondo, ndi zaumulungu.” Anafa mu tchimo Chilango cha imfa chinaperekedwa kwa anthu onse chifukwa cha uchimo, umene umalekanitsa kwamuyaya anthu ndi Mulungu. Aroma 3:23 amatiphunzitsa kuti, “pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu;” M’chikondi chake, Mulungu anakonza njira kuti chilengedwe chake chiomboledwe ku temberero la uchimo ndi imfa. Iye anatumiza Mwana wake, Yesu, ndiponso Mzimu Woyera kuti asinthe moyo wa munthu kuchoka ku imfa kupita ku moyo. “Koma mwa kukoma mtima kwake kwaulere, anthu amapezeka kuti ngolungama pamaso pa Mulungu, chifukwa cha Khristu Yesu amene adawaombola.”

(Aroma 3:24). M’malo motaya mtima, tsopano tili ndi chiyembekezo ndi lonjezo la moyo wosatha kudzera mu mphamvu ya Mulungu yoombola ndi yoyeretsa. “Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Khristu Yesu Ambuye wathu” (Aroma 6:23).

Uthenga Wabwino wa chiyembekezo

Mfundo yaikulu ya uthenga wabwino ndiyo kuitana kwakuti, “Chifukwa chake lapani, tembenukani, kuti afafanizidwe machimo anu” (Machitidwe 3:19). Kutembenuka kumatanthauza kusintha kwakukulu, kutembenuka kwathunthu. Kumaongolera moyo wa munthu, zizolowezi zake, nzeru zake, ndi njira zake. Moyo wosakonzeka umatsogolera ku chionongeko chamuyaya. Yesu anati, “Ngati simutembenuka...simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba” (Mateyu 18:3).

Mankhwala a uchimo

Kodi mankhwala a uchimo ndi chiyani? Kodi munthu angasiye bwanji zilakolako za thupi ndi zilakolako zomwe zimatsogolera moyo? Zimafunika kulowererapo kwaumulungu kuti kubadwa kwauzimu kutheke. Yesu

anauza Nikodemo pa Yohane 3:3-6, “Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sangathe kuona Ufumu wa Mulungu...Chobadwa m’thupi chikhala thupi, ndipo chobadwa mwa Mzimu, chikhala mzimu.” Kupitirira pa kubadwa kwachilengedwe, pali kubadwa kwauzimu komwe kumasintha ndi kusanduliza mzimu wa munthu. Kubadwa mwa uzimu kumasonyeza chozizwitsa cha moyo monga kubadwa kwaumunthu. Mulungu amasintha zinthu zonyansa, zosalungama, ndi zoipitsidwa ndi uchimo kuti zikhale zoyera, zaukhondo, ndi zaumulungu. Mtumwi Petro akunena za kubadwanso kumeneku pa 1 Petro 1:23: “inu amene mudabadwanso, osati ndi mbeu yofeka, komatu yosaola, mwa mau a Mulungu amoyo ndi okhalitsa.” Kubadwa kwauzimu kumeneku sikuchokera ku mbadwo wapadziko lapansi, umene umathera mu imfa, koma m’Mau a Mulungu, amene amapereka moyo.

Chozizwitsa cha chipulumutso

Pamene munthu wavomereza Yesu Khristu ngati mpulumutsi wake, Mulungu amachita chozizwitsa, nausintha moyowo. “Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano” (2 Akorinto 5:17). Mphamvu ya uchimo yathyoledwa, ndipo ungwiro ndi chiyero zimabwezeretsedwa kudzera mu kubadwa kwauzimu kumeneku. Wokhulupirira sapitirira mu uchimo koma amaulamulira kudzera mu mphamvu yakubadwa mwatsopano. Mneneri Yesaya akulongosola za kuyeretsedwa kumene kukuchitika mu izi kuti: “ngakhale zoipa zanu zili zofiira, zidzayera ngati matalala; ngakhale zili zofiira ngati kapezi, zidzakhala ngati ubweya wa nkhosa, woti mbuu.” Mulungu amatsukanso ndi kuyeretsa moyo mu kubadwa kwauzimu kumeneku.

Kubadwa mwauzimu

Malemba amakamba za kubadwa kwauzimu akamanena za kubadwanso mwatsopano, kukonzedwanso, kutsitsimuka, kapena kubadwanso. Pa Tito 3:5 akuti, “zosati zochokera m’ntchito za m’chilungamo, zimene tidazichita ife, komatu monga mwa chifundo chake anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera.” Dongosolo lathunthu la chiombolo ndi chipulumutso limakhudza kuyeretsedwa kwa moyo ku uchimo ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.

(Yapitirira pa tsamba 6)

Izi zimabweretsa kusinthika kwa moyo. Ezekiele analosera za chinthu chodabwitsachi: “Ndipo ndidzakuwazani madzi oyera, ndipo mudzakhala oyera; ndidzakuyeretsani kukuchotserani zodetsa zanu zonse, ndi mafano anu nonse. Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga m’kati mwanu mzimu watsopano; ndipo ndidzachotsa mtima wamwala m’thupi, ndi kukupatsani



“Pokhala anthu, tili ndi mphamvu komanso zofooka monga mwa chibadwidwe, koma pamene moyo wathu watembenuka, pali mphamvu yochokera kwa Mulungu yolimbana ndi uchimo wa umunthu umene kale unkatilekanitsa ndi Iye.”

mtima wamnofu. Ndipo ndidzaika mzimu wanga m’kati mwanu, ndi kukuyendetsani m’malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi kuwachita” (Ezekiele 36:25-27). Matamando akhale kwa Mulungu! Ambuye amatiyeretsa ndi mwazi wake ndi madzi a Mau. Iye amachotsa mtima wakale, wouma, wochimwa ndikuika Mzimu wake mkati mwathu. Kubadwa kwauzimu kumeneku kumatipatsa mphamvu kuti titsate njira za Ambuye ndikukhala moyo wachiyo.

Zochokera kwa Mulungu yekha

Ngakhale kuti munthu mwakufuna kwake akuyenera kutsegulira mtima wake kwa Mulungu kuti akhoza kuona kusinthika kwauzimu kumeneku, palibe chiganizo kapena cholinga cha munthu chimene pachokha chingabweretse kusintha

kwaumulungu kwa moyo wauchimo. Kubadwanso kwauzimu koono kumachokera kwa Mulungu yekha, osati kudzera mu cholowa chilichonse chauzimu kapena dziko. Monga momwe Yohane 1:12-13 amanenera, awo amene amasanduka ana a Mulungu “amene sanabadwe ndi mwazi, kapena ndi chifuniro cha thupi, kapena ndi chifuniro cha munthu, koma cha Mulungu.” Chipulumutso sichimagulidwa kapena kupezedwa mwa kuyesetsa kwaumunthu. “Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro; ndipo ichi chosachokera kwa inu, chili mphatso ya Mulungu: chosachokera ku ntchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense” (Aefeso 2:8-9).

Osati mwa ntchito zathu

Anthu ambiri amafunafuna moyo wauzimu ndi chiombolo kudzera m’zochita zao, ntchito zabwino, makhalidwe abwino, kapena mu chipembedzo. Komabe, moyo ndi chiyero chenicheni umapezeka kokha kupyolera mu ntchito yaumulungu ya Mulungu. “Podziwa kuti simunaomboledwa ndi zovunda, golide ndi siliva, kusiyana nao makhalidwe anu achabe ochokera kwa makolo anu: koma ndi mwazi wa mtengo wake wapatali monga wa mwanawankhosa wopanda chilema, ndi wopanda banga, ndiwo mwazi wa Khristu” (1 Petro 1:18-19). Kumamatira ku miyambo, zikhalidwe, ngakhaleenso miyeso

yapamwamba ya makhalidwe abwino sikungatipangitse kukhala ovomerezeka kwa Mulungu. Chiombolo ndi choposa mphamvu za munthu; ndipo zimatengera mphamvu ya Mlengi kuti ayambitse kubadwa kwauzimu.

Munthu wauzimu

Ife timakhala ndi moyo monga zolengedwa zakuthupi ndi zauzimu. Ngakhale kuti munthu wakunja adzaonongeke ndi matenda ndi imfa, “wa m’kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku” (2 Akorinto 4:16). Paulo akunena za munthu wauzimu pa Akolose 3:9-10: “popeza mudavula munthu wakale pamodzi ndi ntchito zake, ndipo munavala watsopano, amene alikukonzeka watsopano, kuti akhale nacho chizindikiritso, monga mwa chifaniziro cha Iye amene anamlenga iye.” Munthu wakale, wauchimo wachoka ndipo m’ malo mwake pali munthu watsopano, wolengedwa mu chifanizo cha Mulungu.

Otenga nawo mbali pa chikhalidwe chaumulungu

Cholinga cha chipulumutso ndicho kuwachotsa anthu kuchoka mu chikhalidwe cha uchimo ndi kupita ku chikhalidwe changwiro. Kubadwa kwauzimu kumeneku kumabweretsa kusintha kwakukulu mu chikhalidwe ndi mu zochitika. “Kuti mwa izi mukakhale oyanjana nawo umunthu waumulungu, mutathawa chivundi chili m’dziko lapansi mwa chilakolako” (2 Petro 1:3-4). Pamene tikadali ndi zilakolako komanso mayesero aumunthu, pamayenera kukhala kusintha kwa chikhalidwe chabwino. Aefeso 4:24 amatilangiza kuti, “nimuvale munthu watsopano, amene analengedwa monga mwa Mulungu, m’chilungamo, ndi m’chiyero cha choonadi.”

Chitsimikizo cha kubadwa mwatsopano

Pokhala anthu, tili ndi mphamvu komanso zofooka monga mwa chibadwidwe, koma pamene moyo wathu watembenuka, pali mphamvu yochokera kwa Mulungu yolimbana ndi uchimo wa umunthu umene kale unkatilekanitsa ndi Iye. Umboni wa kubadwa mwatsopano wafotokozedwa mu 1 Yohane: “Yense wobadwa kuchokera mwa Mulungu sachita tchimo” (1 Yohane 3:9); “Pakuti chilichonse chobadwa mwa Mulungu chiligonjetsa dziko lapansi” (1 Yohane 5:4); “Muzindikira kuti aliyensenso wakuchita chilungamo abadwa kuchokera mwa Iye” (1 Yohane 2:29). Izi zikutanthauza kusintha kwakukulu kwa kumbali ya makhalidwe ndi moyo wauzimu.

Kudziwika ndi kukula mwa Khristu

Monga momwe ana obadwa mwathupi amatengera chibadwa cha makolo awo nayamwira makhalidwe awo, choteronso iwo amene abadwa mwatsopano. Aefeso 3:15 amanena kuti banja lonse la kumwamba ndi padziko lapansi limatchedwa ndi dzina la Atate. Monga Akhristu obadwa mwatsopano, timadzifananitsa ndi Mulungu; ndipo zokhumba zathu zimagwirizana ndi chifuniro chake. Monga momwe mwana wobadwa kumene amakula nakhala wamkulu, chomwechonso munthu wobadwanso mwauzimu amakula. “koma ndi kuchita zoona mwa chikondi tikakule m’zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu ndiye Khristu” (Aefeso 4:15). Ngakhale kuti kukula kumeneku uli ulendo wa moyo wathu wonse, palibenso madalitso ena aakulu kuposa amene amabwera chifukwa munthu wabadwanso mwatsopano. ■



Kodi mau akuti “kubadwa mwa madzi” pa Yohane 3:5 amanthauza chiyani?

Mu Yohane 3, pa kukambirana kwa Yesu ndi Nikodemo pa nkhanu ya kubadwa mwatsopano, palinso mau akuti, “Ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sangathe kulowa ufumu wa Mulungu.” Mau akuti ‘madzi’ pa ndimeyi amatengedwa ngati osamveka bwino pa zaumulungu ndipo amanthauziridwa mosiyanasiyana.

Mau amene anenedwawa anabwera potsatira funso limene Nikodemo anafunsa lakuti kodi iye alowenso m’mimba mwa amai ake kuti akabadwenso. Pali matanthauzidwe atatu omwe ndiwalingalire mwachidule.

1. Kubadwa mwathupi: ‘Kubadwa mwa madzi’ kunganthauze kubadwa mwakuthupi. Kubadwa koyamba ndi kubadwa kwachilengedwe kwa madzi, ndipo kubadwa kwachiwiri ndiko kubadwa kwauzimu mwa mzimu. Yesu akusiyanyitsa ziwirizo ponena kuti: “Chobadwa m’thupi chikhala thupi; ndipo chobadwa mwa Mzimu, chikhala mzimu.” Mau awa akusiyanyitsa za chathupi ndi chochokera uzimu.

2. Kuyereetsa mophiphiritsa: Mu Malemba, madzi nthawi zambiri amagwiritsidwa ntchito kuimira kuyereetsa ndi kusambitsidwa. Aefeso 5:26 amanena za Khristu kuti adzayeretsa mpingo mwa “kumsambitsa madzi ndi mau.” Chimodzimodzi pa Ezekiele 36:25-27 amati: “Ndipo ndidzakuwazani madzi oyera, ndipo mudzakhala oyera...ndipo ndidzaika mzimu wanga m’kati mwanu.” Kugwiritsidwa ntchito kwa ‘madzi’ ndi ‘mzimu’ monga pa Yohane 3:5 kukhoza kuimira zenizeni zauzimu. Yesu ananena mu Yohane 15:3, “Mwakhala okonzeka tsopano inu chifukwa cha mau...” Paulo ananenanso za Akhristu amene “anasambitsidwa” (1 Akorinto 6:11). Kubadwa mwatsopano ndiko kubadwa kuchokera kumwamba, zomwe zingasonyeze kuti madzi ndi mzimu zomwe zikunenedwazo zikanakhala njira za Mulungu zauzimu. Chifukwa chaichi, kubadwa mwatsopano kudzabwera mwa kuyereetsedwa kwauzimu kwa Mau ndi Mzimu wa Mulungu.

3. Tanthauzo lolakwika la ubatizo: Lingaliro lachitatu likuyerekeza mokhala ngati kulakwitsa kuti “kubadwa m’madzi” ndi ubatizo wachikhristu, kutanthauza kuti ubatizo ndi wofunikira kuti munthu apulumuke. Komabe, izi zimatsutsana ndi mfundo yakuti chipulumutso ndi ntchito yaumulungu, osati ntchito ya munthu. Monga mwa Malemba, ubatizo ndi ntchito yakunja ya munthu imene itsimikizira za ntchito ya mkati ya Mulungu. Chigawenga pamtanda paja sichinabatizidwe koma chinalonjezedwa kukakhala ku paradiso. Uwu ndi umboni weniweni wakuti zimenezi sizikutanthauza ubatizo wa m’madzi.

Njira zisanu zopezera chipulumutso

Kubadwa kwauzimu ndi ntchito imene Mulungu amaichita mu moyo. Ngakhale kuti sizichitika ndi ntchito zathu, tiyenera kukwaniritsa zinthu zina kuti Mulungu atipatse kusintha kodabwitsaku. “Chipulumutso ncha Yehova” (Yona 2:9).

Imvani Uthenga

Aroma 10:17 Motero munthu amakhulupirira chifukwa cha zimene wamva, ndipo zimene wamvazo zimachokera ku zolalika za Khristu.

Khulupirani Yesu monga Mwana wa Mulungu

Yohane 3:16 Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi koteru, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakuhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha.

Itanirani pa Mulungu

Aroma 10:13 Pakuti, aliyense amene adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.

Vomerezani

1 Yohane 1:9 Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse.

Lapani tchimo

Machitidwe a Atumwi 3:19 Chifukwa chake lapani, bwererani kuti afanizidwe machimo anu.



KODI MUKUDZIWA?

Nikodemo, Mfarisi, amatchulidwa mwapaderadera mu Uthenga Wabwino wa Yohane wokha. Iye sanatchulidwe m'mauthenga ena aliwonse. Nkhani yake ikupezeka mu zochitika zazikuluzikulu zitatu:

1. Kukambirana kwake kwakukulu ndi Yesu pa za kubadwanso mwauzimu (Yohane 3:1-21).
2. Iye anamuteteza Yesu, nalimbikitsa Afarisi anzake kuti amve kaye mulandu wake pamaso pa bwalo lalikulu la Ayuda molingana ndi malamulo a Ayuda (Yohane 7:50-51).
3. Mchitidwe wake wodzipereka, pamene iye ndi Yosefe wa ku Arimateya anadzoza thupi la Yesu ndi mafuta a mure ndi aloe kenako ndikukaliika m'manda (Yohane 19:38-42).



**Mau a
Nyengo
Yake**

MDALITSO WA ANA A MULUNGU

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Nena ndi Aroni ndi ana ake, ndi kuti, Uzidalitsa ana a Israele motero. — Numeri 6:23

Mulungu anapatsa Mose malangizo a mmene Aroni, mkulu wa ansembe, anayenera kuperekerana mdalitso waukulu pa ana a Israele. Pemphero ili lomveka bwino ndilo mdalitso ndipo likuonetsa mtima wa Mulungu Mwiniwake:

Yehova akudalitse iwe, nakusunge; Yehova awalitse nkhope yake pa iwe, nakuchitire chisomo; Yehova akweze nkhope yake pa iwe, nakupatse mtendere. (v. 24-26).

Chikhumbo cha Mulungu chofuna kudalitsa ana ake sichinagwedezekere mpaka pano. Madalitso enieni amachokera kwa Mulungu yekha, amene ali Namalenga. Dalitso limeneli limaonetsera chimene Mulungu akufunabe kuchitira ana ake lero lino.

Chipulumutso sichipangitsa kuti anthu asadutse m'mazunzo ndi m'zovuta. Nthawi zina mitima yathu imalira ndi zolemetsa zomwe moyo umabweretsa. Mnyengo zimenezo, tiyeni tikweze maso athu kupyola mavuto ooneka ndi kutembenukira kwa Yehova. Kumbukirani kuti mtima wake umakhudzidwa ndi zofooka zathu. Mvetserani ku liwu lodekha, laling'ono la Mzimu pamene Iye akutitsimikizira:

Ndidzakudalitsa. Ndidzakutetezani ndi kukhala pothawirapo pako mu namondwe. Ndidzakusamalira ndi kukutsogolera ndi kuunika kwanga. Ndidzakhala wokoma mtima ndi wachifundo. Ndidzakukuta ndi kupezeka kwanga ndipo ndidzakupatsa mtendere.

Iyi si ndakatulo chabe, koma ndi mdalitso umene Mulungu amapereka kwa ana ake. Pamene mitu yathu yaweramira pansu ndipo zothodwetsa zikulemetsa mitima yathu, tikumbukire chikhumbo cha Mulungu chotalitsa. Polimbikitsidwa mkati, odzazidwa ndi mtendere wa Mulungu, wophimbidwa ndi chifundo chake, ndi kukumbatiridwa ndi chikondi cha Mulungu, tili okonzeka kupita kugawana nawo mdalitso umenewu ndi dziko lapansi.

Tikhoza kuwatsimikizira ena za chikondi ndi chithonhozo chake, ndipo tikhoza kuwadalitsa iwo monga momwe Aroni anadalitsira ana a Israele m'dzina la Yehova. Sitili tokha; sanatsiyiye opanda chithonhozo. M'malo mwake, tikhoza kudzuka, titapatsidwa mphamvu ndi chisomo cha Mulungu, kuti tili okonzeka kukhala zotengera za madalitso ake.

Tiyeni tipite chitsogolo, ndipo tipereke mtendere umene upambana chidziwitso chonse, chikondi chimene sichiona malire, komanso chithonhozo chimene chimatigwiriziza ngakhale mu nthawi yamdima wandiweyani. Tikhale njira za chisomo cha Mulungu ndipo kuwala kwa nkhope yake kuwalira ife pamene tikuyenda mu mphamvu ya Mulungu. ■

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

